
2021

Ndikoyenela kuti amayi onse akhale ndi owayang'anira amene iwo asankha okha panthawi ya matenda,pobereka,komaso nthawi imene mwana wagobadwa kumene

Breakthrough RESEARCH

Follow this and additional works at: https://knowledgecommons.popcouncil.org/focus_sexual-health-repro-choice

[How does access to this work benefit you? Click here to let us know!](#)

Recommended Citation

Breakthrough RESEARCH. 2021. "Ndikoyenela kuti amayi onse akhale ndi owayang'anira amene iwo asankha okha panthawi ya matenda,pobereka,komaso nthawi imene mwana wagobadwa kumene." Washington, DC: Population Council.

This Poster is brought to you for free and open access by the Population Council.

NDIKOYENELA KUTI AMAYI ONSE AKHALE NDI OWAYANG'ANIRA AMENE IWO ASANKHA OKHA PANTHAWI YA MATENDA, POBEREKA, KOMASO NTHAWI IMENE MWANA WAGOBADWA KUMENE

Kuthandizidwa maganizo: kulimbikitsa mtima pamene mzimayi oyembekezera ali munthawi yofuna kuchira



- ✓ Kumulimbikitsa komaso kumosisita pamsana pamene uluru wachulukuka kuti uluru uchepe
- ✓ Kuwapukuta amayi oyembekezera thupi lawo lonse ndikamsalu konyowa kuti amve mphepo yabwino
- ✓ Kambiranani ndi mzimayi oyembekezera pazomwe zikuchitika and onetsetsani kuti wamvetsetsa zomwe mzamba wakuchipatala akufotokoza
- ✓ Mulimbikitseni mzimayi amene wabwera kudzachira kukodza maola awiri aliwonse ndiposo kusamba pamene matenda ayamba ngati wasankha kutero
- ✓ Ndibwino mzimayi amene matenda ayamba kukhala ndi munthu omudikilira komaso omuthandizira kuyenda pomwe matenda ayamba
- ✓ Muthandizireni mzimayi kuti akhale opanda mantha komaso kumuphunzitsa kapumidwe kabwino pamene matenda awawa

Kulankhulana



- ✓ Mumvetsetse malangizo a azamba ndipo wonetsetsani kuti mayi oyembekezera wamvetsetsa malangizowo
- ✓ Muthandizireni mzimayi oyembekezera kuti afunse mafunso okhudzana chisamaliro chake ndipo wonetsetsani kuti wapeza umphungu onse omwe amayenera kulandira
- ✓ Wonetsetsani kuti azamba akumvetsetsa ndi kupereka zofunika kwa mzimayi oyembekezera monga ngati mankhwala othandizira uluru

Chakudya ndi madzi



- ✓ Konzani ndikusunga chakudya ndi madzi pafupi, pamene chakudya chafunikira athandiziren kuwadyetsa komaso kuwamwetsa madzi

Zoyang'anira

- ✓ **Kutaya magazi:** pamene mzimayi wachira kumene ndibwino kumufunsa pafupipafupi ngati akutaya magazi komaso kuti ayang'ane malo ogona ngati akutaya magazi Adziwitseni azamba pamene mwaona kuti akutaya maagazi.
- ✓ **Zizindikiro zina zoopsa:** Pamene mzimayi oyembekezera akumva zizindikiro ngati chizumba zumba, kufooka kapena kumva ngati afuna kukomoka adziwitseni azamba



Chisamaliro cha mwana

- ✓ Onetsetsani kuti thupi lamwana ndi lamayi wake ndilogundana nthawi zonse pamene wabadwa kumene
- ✓ Limbikitsani kuyamwitsa mwana pomwe wabadwa kumene
- ✓ Muwadziwitse pamene mwaona magazi pamchombo pa mwana komaso panthawi yomwe mwaona kuti akuvutika kupuma
- ✓ Athandizireni azamba pachisamaliro chamwana komaso kumveka dzovala
- ✓ Muthandizireni mzimayi kuyamwitsa mwana msanga komaso pafupi pafupi
- ✓ Musamulekenitse mwana kwa mayi wake pokhapokha a chipatala atakuuzani



Kukhala othandizira

- ✓ Mukuyenera kunkhala pafupi ndi chipinda chochiliramo azimayi oyembekezera ndikuwathandiza anamwino pamene pafunika kutero
- ✓ Akumbutseni azamba nthawi yomwe akuyenela kudzamuunika odwala



Wonyamula muuni

- ✓ Yatsani muuni wanu pamene amzamba akuwaona amayi oyembekezera komaso panthawi yomwe akuchira

